| Chichewa | English |
|---|---|
| **(Panting) A nurse ndabwelanso ndi mwana wanga, angonjenjemera, koma thupi liri moto buuu, kusanza mkati! Komanso bambo ake akuwononga ndalama zambiri kudwazika matenda pafupipafupi.** | Nurse, I have come with my child. She is shivering and the body temperature seems so high. She is also vomiting. Her father is spending a lot of money because of her persistent illnesses |
| **Ndimalungotu amenewa, dziwani kuti matenda a malungo ndi owopsya ndipo  amapha makamaka kwa ana chonchi. Kodi mukudwiwa kuti mukhoza kupewa malungo pogona M'masikito onyikidwa m'mankwala usiku uli wonse?** | This is Malaria, know that malaria is dangerous especially to children like these and it kills. Do you know that you can prevent Malaria by sleeping under a treated mosquito net every night? |
| **Zamasikito ndinamva a nurse, koma sizodulanso zimenezo. Kaya bambo angakwanitse kugula?** | Nurse, I have heard about mosquito nets but are they not expensive? Can my husband afford to buy them? |
| **Masikito siwodula ayi ndipo akupezeka mzipatala zaboma ndi za ission pamtengo wotsika kwa amayi oyembekezela ndi ana ochepela zaka zisanu. Kuchipatala kononso masikitowa alipo. Kawalimbitseni bambo kuti asunge ndalama kuti nanu mudzamgulile mwanayu masikitowa.** | Mosquito nets are not expensive and they are found in government and mission clinics at a low price of k50 only for pregnant women and children under the age of five. Even here (at the clinic) there are nets. Encourage your husband to save money for you to buy the net for this child. |
| **Malungo ndi oopsa ndipo amapha! Koma kupewa malungo kuli mmanja mwanu. Ana aang'ono ndi amayi oyembekezera ali pachiopyezo cha malungo choncho atetezeni nthawi zonse ku malungo. Pewani kutaya ndalama ndi nthawi podwazika matenda; Gonani mmasikito wonyikidwa m'mankwala usiku uliwonse, chaka chilichonse!** | Malaria is dangerous and it kills! But the way of preventing it lies in your hands. Children and pregnant women are most at risk of getting Malaria, therefore, make an effort to protect them all the time. Avoid spending a lot of money and time through taking care of people who are sick. Sleep under a treated net every night, each and every year. |

| Chichewa | English |
|---|---|
| **Kodi mwamaliza kukonza pogonapa……** | Have you finished making up the place (preparing where to sleep) |
| **Eee! Bwanji?** | Yes! Why asking that? |
| **Simunamalize, Chitetezo net chili kuti apa…** | You haven't finished, where is the chitetezo net here? |
| **Masikitonso a chiyani, nyengo ya mvula siyatha, udzudzu sukusokosanso.** | What for? The rainy season is over and mosquitoes are not making noise |
| **Anakuuzani kuti udzudzu opereka malungo umakhala nthawi ya mvula yokha ndani?.....malungo mai alibe nyengo. Udzudzu ofalitsa malungo siusokosa ayi ndipo umapeleka malungo usiku uliwonse chaka chonse. Kugona mu chitetezo net ndikofunika ngati m'mene mumatungila madzi pa nyumba. Mmmatunga madzi tsiku ndi tsiku…Tiyeneranso kugona mu Chitetezo neti usiku uli wonse komanso chaka chilichonse.** | Who told you that the mosquito that transmits malaria is found during the rainy season only? Malaria has no season. The mosquito that transmits malaria does not make noise and is capable of transmitting malaria every night all year round. Sleeping under the net is as important as drawing water at home. You draw water every day…you should also sleep under a treated net every night each and every year. |
| **Zikomo bambo zamveka. Ndipo zoona tingathe kupewa malungo. Komanso Chitetezo neti sichovuta kumanga ndikugwirita ntchito! Basi ndikupita ku chipinda kwa anaku ndikawamangile Chitetezo neti chawo.** | Thank you very much. It's true we can prevent malaria and Chitetezo Net is not difficult to hang and use. I will go straight to the children's bedroom to put up the net for them |
| **Kupewa malungo kuli mmanja mwathu. Gonani mu Chitetezo neti usiku ulionse, chaka chilichonse.** | Prevention of malaria is in our hands/it's our responsibility. Sleep under the net every night all year round |
| **CHITETEZO NETI! USIKU ULIONSE, CHAKA CHILI CHONSE!** | **CHITETEZO NETI! EVERY NIGHT EACH AND EVERY YEAR** |